# Maphunziro a m’Baibulo

Bible studies

# Kukwera Kumwamba kwa Yesu ndi zimene zinacitika kucokera pa nthawi iyo

1. Yesu akwera kunka Kumwamba
2. Tsiku la Pentekoste
3. Petro apulumuka m’ndende
4. Kusandulika mtima kwa Paulo
5. Mdindo wa ku Filipi

# 1. Yesu akwera kunka Kumwamba

**Macitidwe a Atumwi 1.4-14**

4. ndipo posonkhana nao pamodzi, anawalamulira asacoke ku Yerusalemu, komatu alindire lonjezano la Atate, limene, anati, munalimva kwa Ine;
5. pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri.
6. Pamenepo iwowa, atasonkhana pamodzi, anamfunsa Iye, nanena, Ambuye, kodi nthawi yino mubwezera ufumu kwa Israyeli?
7. Koma anati kwa iwo, Sikuli kwa inu kudziwa nthawi kapena nyengo, zimene Atate anaziika m'ulamuliro wace wa Iye yekha.
8. Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu; ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko.
9. Ndipo m'mene adanena izi, ali cipenyerere iwo, ananyamulidwa; ndipo mtambo unamlandira Iye kumcotsa kumaso kwao.
10. Ndipo pakukhala iwo cipenyerere kumwamba pomuka Iye, taonani, amuna awiri obvala zoyera anaimirira pambali pao.
11. amenenso anati, Amuna a ku Galileya, muimiranji ndi kuyang'ana kumwamba? Yesu amene walandiridwa kunka


Kumwamba kucokera kwa inu, adzadza momwemo monga munamuona alinkupita Kumwamba.
12. Pamenepo anabwera ku Yerusalemu kucokera ku phiri lonenedwa la Azitona, limene liyandikana ndi Yerusalemu, loyendako tsiku la Sabata.
13. Ndipo pamene adalowa, anakwera ku cipinda ca pamwamba, kumene analikukhalako; ndiwo Petro ndi Yohane ndi Yakobo ndi Andreya, Filipo ndi Tomasi, Bartolomeyu ndi Mateyu, Yakobo mwana wa Alifeyu, ndi Simoni Zelote, ndi Yuda mwana wa Yakobo.
14. Iwo onse analikukangalika m'kupemphera, pamodzi ndi akazi, ndi Mariya, amace wa Yesu, ndi abale ace omwe.

**Mafunso**

1. Kodi Ambuye Yesu analonjeza ophunzira ace cibatizo cotani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Ndi kuti kumene ophunzira a Yesu anayenera kulalikira Mau a Mulungu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Ndi ciani cimene cinacitina pambuyo pace Ambuye Yesu adalangiza ophunzira ace? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Ndi yani amene anaimirira pafupi ndi ophunzira? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi angelo ananena ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi ophunzira anapita kuti pambuyo pace? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi iwo anacita ciani komweko? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
8. Angelo ananena kuti Yesu adzabweranso. Kodi mumayembekezera Yesu kubweranso pa nthawi iliyonse?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao ndipo pezani yankho




SABATA
GALILEYA
MTAMBO
MPHAMVU
ISRAYELI
YERUSALEMU

MADZI
UFUMU
KUMWAMBA
SAMARIYA
KUPEMPHERA

## 2. Tsiku la Pentekoste

**Yohane 14.15-17**

15. Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga.
16. Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo akdzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi yonse.
17. ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona Iye, kapena kumzindikira Iye. Inu mumzindikira Iye; cifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu.

**Macitidwe a atumwi 2.1-13**

1. Ndipo pakufika tsiku la Pentekoste, anali onse pamodzi pa malo amodzi.
2. Ndipo mwadzidzidzi anamveka mau ocokera Kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba, nadzaza nyumba yonse imene analikukhalamo.
3. Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekha wayekha.
4. Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa.
5. Koma anali m'Yerusalemu okhalako Ayuda, amuna opembedza ocokera ku mtundu uli wonse pansi pa thambo.
6. Koma pocitika mau awa, unyinji wa anthu unasonkhana, nusokonezedwa, popeza yense anawamva alikulankhula m'cilankhulidwe cace ca iye yekha.
7. Ndipo anadabwa onse, nazizwa, nanena, Taonani, awa onse alankhulawa Sali Agalileya kodi?
8. Ndipo nanga ife timva bwanji, yense m'cilankhulidwe cathu cimene tinabadwa naco?
9. Aparti ndi Amedi, ndi Aelami, ndi iwo akukhala m'Mesopotamiya, m'Yudeya, ndiponso m'Kapadokiya, m'Ponto, ndi m'Asiya
10. m'Frugiya, ndiponso m'Pamfuliya, m'Aigupto, ndi mbali za Libiya wa ku Kerene, ndi alendo ocokera ku Roma, ndiwo Ayuda, ndiponso opinduka
11. Akrete, ndi Aarabu, tiwamva iwo alikulankhula m'malilime athu zazikuru za Mulungu.
12. Ndipo anadabwa onse, nathedwa, nzeru, nanena wina ndi mnzace, Kodi ici nciani?
13. koma ena anawaseka nanena kuti, Akhuta vinyo walero.

**Mafunso**

1. Werenganinso Yohane 14.15-17. Kodi Ambuye Yesu analonjeza ciani kwa ophunzira ace kulingana ndi ndime izi?
2. Kodi mau ocokera Kumwamba omwe ophunzira anamva anali monga ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi anthu anaona ciani pa mitu ya ophunzira? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi ophunzira analankhula ndi malilime angati? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Anthu ena anaseka ophunzira. Kodi anthuwo anati ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi?

**Sewero**

Pezani mau ndipo lembani yankho mogwiritsa nchito malembo osaphedwa

| | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | M | A | W | M | U | K | E |
| Y | N | I | D | A | N | O | O | C |
| U | T | E | K | O | T | O | M | U |
| D | O | M | P | H | E | P | O | A |
| A | E | M | I | L | I | L | A | M |
| E | W | S | O | H | K | N | S | T |

NKHOSWE COONADI
KUMWAMBA MAU
MPHEPO MALILIME
MOTO AYUDA

P _ _ _ _ _ _ _ _ E

## 3. Petro apulumuka m'ndende

**Macitidwe a Atumwi 12.5-16**

5. Pamenepo ndipo Petro anasungika m'ndende; koma Eklesia anampempherera iye kwa Mulungu kosalekeza.
6. Ndipo pamene Herode anati amturutse, usiku womwewo Petro analikugona pakati pa asilikari awiri, womangidwa ndi maunyolo awiri; ndipo alonda akukhala pakhomo anadikira ndende.
7. Ndipo taonani, mnge lo wa Ambuye anaimirirapo, ndipo kuunika kunawala mokhalamo iye; ndipo anakhoma Petro m'nthiti, namuutsa iye, nanena, Tauka msanga. Ndipo maunyolo anagwa kucoka m'manja mwace.
8. Ndipo mngelo anati kwa iye, Dzimangire m'cuuno, numange nsapato zako. Nacita cotero. Ndipo ananena naye, Pfunda cobvala cako, nunditsate ine.
9. Ndipo anaturuka, namtsata; ndipo sanadziwa kuti ncoona cocitidwa ndi mngelo, koma anayesa kuti alikuona masomphenya.
10. Ndipo m'mene adapitirira podikira poyamba ndi paciwiri, anadza ku citseko cacitsulo cakuyang'ana kumudzi; cimene cidawatsegukira cokha; ndipo anaturuka, napitirira khwalala limodzi; ndipo pomwepo mngelo anamcokera.
11. Ndipo Petro atatsitsimuka, anati, Tsopano ndidziwa zoona, kuti Ambuye anatuma mngelo wace nandilanditsa ine m'dzanja la Herode, ndi ku cilingiriro conse ca anthu a Israyeli.
12. Ndipo m'mene adalingirirapo, anadza ku nyumba ya Mariya amace wa Yohane wonenedwanso Marko, pamenepo ambiri adasonkhana pamodzi, ndipo analikupemphera.
13. Ndipo m'mene anagogoda pa citseko ca pakhomo, linadza kudzabvomera buthu, dzina lace Roda.
14. Ndipo pozindikira mau ace a Petro, cifukwa ca kukondwera sanatsegula pakhomo, koma anathamanga nalowanso, nawauza kuti Petro alikuima pakhomo.
15. Koma anati kwa iye, Wamisala iwe. Ndipo analimbika ndi kunena kuti nkutero. Ndipo ananena, Ndiye mngelo wace.
16. Koma Petro anakhala cigogodere; ndipo m'mene adamtsegulira, anamuona iye, nadabwa.

**Mafunso**

1. Kodi Eklesia (anthu okhulupirira Yesu) anacita ciani pamene Petro anakhala mu ndende? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Nanga inu mumacita ciani mukabvutika?
3. Petro anagona m'ndende cifukwa sanaope. Ndi cifukwa ciani sanaope kulingana ndi inu?
4. Kodi Petro anacoka bwanji m'ndende? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

5. Kodi ndi cotheka bwanji kuti asilikali sanaone Petro ndi mngelo?
6. Kodi Petro anapita kuti atamasulidwa m'ndende? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi Roda anacita ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
8. Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi?

**Sewero**
Lembani malembo pa malo ao kukapeza yankho lolembedwa m'Salimo 28.7.

| 25 | 5 | 8 | 15 | 22 | 1 | | 14 | 4 | 9 | 25 | 5 | | 13 | 16 | 8 | 1 | 13 | 22 | 21 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | | | | | | | | |

| 25 | 1 | 14 | 7 | 1 | | 14 | 11 | 9 | | 3 | 9 | 11 | 15 | 16 | 1 | | 3 | 1 | 14 | 7 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | | | | | | | | | | |

| 13 | 20 | 9 | 13 | 1 | | 23 | 1 | 14 | 7 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | |

| 23 | 1 | 11 | 8 | 21 | 12 | 21 | 16 | 9 | 18 | 9 | 18 | 1 | | 9 | 25 | 5 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | | | | | |

| 14 | 4 | 9 | 16 | 15 | | 1 | 14 | 1 | 14 | 4 | 9 | 20 | 8 | 1 | 14 | 4 | 9 | 26 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | | | | | | | | |

| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |

| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | z |

## 4. Kusandulika mtima kwa Paulo

**Macitidwe a Atumwi 9.1-18**
1. Koma Saulo wosaleka kupumira pa akuphunzira a Ambuye kuopsya ndi kupha, ananka kwa mkulu wa ansembe.
2. napempha kwa iye akalata akunka nao ku Damasiko kumasunagoge, kuti akapeza ena otsata Njirayo, amuna ndi akazi akawatenge kudza nao omangidwa ku Yerusalemu.
3. Ndipo poyenda ulendo wace, kunali kuti iye anayandikira Damasiko; ndipo mwadzidzidzi kudawala momzingira kuunika kocokera kumwamba;
4. ndipo anagwa pansi, namva mau akunena naye, Saulo Saulo, Undilondalonderanji?
5. Koma anati, Ndinu yani Mbuye? Ndipo anati: Ndine Yesu amene umlondalonda;
6. komatu, uka, nulowe m'mudzi, ndipo kudzanenedwa kwa iwe cimene uyenera kucita.
7. Ndipo amunawo akumperekeza iye anaima du, atamvadi mau, koma osaona munthu.
8. Ndipo Saulu anauka; koma potseguka maso ace, sanapenya kanthu; ndipo anamgwira dzanja, namtenga nalowa naye m'Damasiko.
9. Ndipo anakhala masiku atatu wosaona, ndipo sanadya kapena kumwa.
10. Koma ku Damasiko kunali wophunzira wina dzina lace Hananiya; ndipo Ambuye anati kwa iye m'masomphenya, Hananiya. Ndipo anati, Ndiri pano, Ambuye.
11. Ndipo Ambuye anati kwa iye, Tauka, pita ku khwalala lochedwa Lolunjika, ndipo m'nyumba ya Yuda ufunse za munthu dzina lace Saulo, wa ku Tariso; pakuti taona, alikupemphera
12. ndipo anaona mwamuna dzina lace Hananiya, alikulowa, namuika manja, kuti apenyenso.
13. Ndipo Hananiya anayankha nati, Ambuye, ndamva ndi ambiri za munthu uyu, kuti anacitiradi coipa oyera mtima anu m'Yerusalemu;
14. ndi kuti pano ali nao ulamuliro wa kwa ansembe akulu wakumanga onse akuitana pa dzina lanu.

15. Koma Ambuye anati kwa iye, Pita; pakuti iye ndiye cotengera canga cosankhika, cakunyamula dzina langa pamaso pa amitundu ndi mafumu ndi ana a Israyeli;
16. pakuti Ine ndidzamuonetsa iye zinthu zambiri ayenera iye kuzimva kuwawa cifukwa ca dzina langa.
17. ndipo anacoka Hananiya, nalowa mnyumbayo; ndipo anaika manja ace pa iye, nati, Saulo, mbale, Ambuye wanditumа ine, ndiye Yesu amene anakuonekerani pa njira wadzerayo, kuti upenyenso, ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera.
18. Ndipo pomwepo padagwa kucoka m'maso mwace ngati mamba, ndipo anapenyanso.
19 ndipo ananyamuka nabatizidwa; ndipo analandira cakudya, naona naco mphamvu.

**Mafunso**

1. Saulo anazunza anthu otsata Njirayo. Ndi Njira yotani?
2. Ndi ciani cimene cinacitika pamene Saulo anali kupita pa njira ya ku Damasiko? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Ndi yani amene anakamba ndi Saulo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Saulo anayankha ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Ndi cifukwa ciani cinali cofunikira kuti amuna anagwira dzanja la Saulo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Ndi cifukwa ciani Hananiya ananyanyala asanapite kwa Saulo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi Hananiya anacita ciani atafika kumene Saulo analiko? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
8. Mulungu anasintha mtima wa Paulo. Kodi asinthanso mtima wanu? Kusandulika mtima ndi kotani?

## 5. Mdindo wa ku Filipi

**Macitidwe a Atumwi 16.16-34**


16. Ndipo panali, pamene tinalinkunka kukapemphera, anakomana ndi ife namwali wina amene anali ndi
mzimu wambwebwe, amene anapindulira ambuye ace zambiri pakubwebweta pace.
17. Ameneyo anatsata Paulo ndi ife, napfuula, kuti, anthu awa ndi akapolo a Mulungu wa Kumwambamwamba, amene akulalikirani inu njira ya cipulumutso.
18. Ndipo anacita cotero masiku ambiri. Koma Paulo anabvutika mtima ndithu, naceuka, nati kwa mzimuwo, Ndikulamulira iwe m'dzina la Yesu Kristu, turuka mwa iye. Ndipo unaturuka nthawi yomweyo.
19. Koma pamene ambuye ace anaona kuti kulingalira kwa kupindula kwao kwatha, anagwira Paulo ndi Sila, nawakokera kunka nao kuwbalo kwa akuru,
20. ndipo pamene adanka nao kwa oweruza, anati, Anthu awa abvuta kwambiri mudzi wathu, ndiwo Ayuda.
21. ndipo alalikira miyambo imene siiloleka ife kuilandira, kapena kuicita, ndife Aroma.
22. Ndipo linagumukira iwo khamulo; ndipo oweruza anawang'ambira maraya ao; nalamulira kuti awakwapule.
23. Pamene anawaonetsa mikwingwirima yambiri anawaika m'ndende, nauza mdindo kuti awasunge bwino.
24. Pakumva iye kulamulira kotero anawaika m'cipinda ca m'kati, namangitsa mapazi ao m'zigologolo.
25. Koma ngati pakati pa usiku, Paulo ndi Sila analinkupemphera,
nayimbira Mulungu nyimbo, ndipo a m'ndendemo analinkuwamva.
26. ndipo mwadzidzidzi panali cibvomezi cacikuru, cotero kuti maziko a ndende anagwedezeka; pomwepo pamakomo ponse panatseguka; ndi maunyolo a onse anamasuka.
27. Pamene anautsidwa kutulo mdindoyo, anaona kuti pa makomo a ndende panatseguka, ndipo anasolola lupanga lace, nati adziphe yekha, poyesa kuti a m'ndende adathawa.
28. Koma Paulo anapfuula ndi mau akuru, nati, Usadzipweteka wekha; tonse tiri muno.
29. Ndipo mdindo anaitanitsa nyali, natumphira m'kati, alinkunthunthumira ndi mantha, nagwa pamaso pa Paulo ndi Sila,
30. nawaturutsira iwo kunja, nati, Ambuye ndicitenji kuti ndipulumuke?
31. Ndipo iwo anati, Ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka, iwe ndi apabanja ako.
32. Ndipo anamuuza iye mau a Ambuye, pamodzi ndi onse a pabanja pace.
33. Ndipo anawatenga ora lomwelo la usiku, natsuka mikwingwirima yao; nabatizidwa pomwepo, iye ndi a pabanja pace.
34. Ndipo anakwera nao kunka kunyumba kwace, nawakhazikira
cakudya, nasangalala kwambiri, pamodzi ndi a pabanja pace, atakhulupirira Mulungu.

**Mafunso**

1. Kodi mkazi amene anali ndi mzimu wambwebwe anacita ciani? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Ndi cifukwa ciani ambuye a mkazi anafuna kuwaika Paulo ndi Sila m’ndende? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi mdindo anacita ciani kuti Paulo ndi Sila asathawe? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
7. Kulingana ndi inu ndi cifukwa ciani Paulo ndi Sila anaimbira Mulungu nyimbo?
8. Ndi ciani cimene cinacitika usiku? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
9. Kodi mdindo anafunsa ciani Paulo ndi Sila? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
10. Nanga inu mufunanso kupulumuka ku macimo anu?
11. Kodi Paulo anamyankha ciani? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
12. Kodi mdindo anacita ciani atabatizidwa? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?

**Sewero**

Lembani mau pa malo ao kukapeza yankho.




| | |
|---|---|
| AROMA | CIPULUMUTSO |
| NYIMBO | LUPANGA |
| MZIMU | MDINDO |
| BANJA | CIPINDA |
| AKAPOLO | SANGALALA |
| AYUDA | PULUMUKA |